CHINDUNJI CHA NKHANI

"MTSOGOLERI SABADWA, AMASULIDWA"

'Mtsogoleri sabadwa; mtsogoleri amasulidwa.' (Rwanda)



UMUNTHU
MMACHITIDWE

Ndondomeko Zotsogozedwa ndi Achinyamata Zolimbikitsira

UMOYO WA MMAGANIZO WA ACHINYAMATA KU M'MAWA KWA AFRICA

The Sawa Project

“Pamene achinyamata apatsidwa mpata, uphungu komanso zoyenera kuti atsogolere, samangotenga nawo gawo kuti zinthu zisinthe, iwo amaongoleranso kusinthako. Nthawi yoyika ndalama mu utsogoleri wa achinyamata ndi ino.”

Peter Ogoi, Mtsogoleri wa Sawa, Kenya

M'chigawo chonse cha ku Mmawa kwa Africa, achinyamata ali kale patsogolo kuchitapo kanthu pamavuto a umoyo wa mmaganizo. Kupanga magulu othandizana wina ndi mzake, kupereka chithandizo, kupanga makanema othana ndi machitidwe osalana, kuyendetsa ma pulogalamu kusukulu, kupanga njira zamakono zamakina a kompuyuta, kumenyera ufulu kuti ndondomeko zisinthe, komanso kufikira anthu m'madera omwe ndondomeko zokhazikika sizifikako kawirikawiri.

Pakati pa 2025-2026, Pulojekiti ya Sawa idabweretsa pamodzi atsogoleri 29 ochokera ku Kenya, Malawi, Rwanda, Somalia, Tanzania ndi Uganda. Owona zam'maganizo, aluso, okonza za m'madera, opanga makanema, komanso omenyera ufulu, adali akugwira kale ntchito zothandiza achinyamata pa nkhani za umoyo wa m'maganizo kumadera komwe thandizo lidali losowa. Pogwiritsa ntchito uphungu, maphunziro, kupanga maubale komanso kupereka thandizo loyambira, atsogoleri a Sawa adapanga komanso kubweretsa mapulojekiti khumi okhudza umoyo wa m'maganizo pakati pa achinyamata, adafikira anthu oposera 2,900 komanso kuwonjezerapo zikwizikwi zomwe zidafikiridwa kudzera pa makina a intaneti.

ZOKHUZA PULOJEKITI YA SAWA

Pulojekiti ya Sawa ndiya miyezi 21 yokhazikitsidwa ndi bungwe la Kofi Annan Foundation mogwirizana ndi bungwe la MCW Global komanso bungwe la Africa Alliance la ma YMCA. Sawa adayika ndalama mwa achinyamata omwe ndi atsogoleri a umoyo wa m'maganizo, azaka zapakati pa 25 mpaka 35, amene akugwira kale ntchito popititsa patsogolo umoyo wa mmaganizo komanso chisamaliro cha achinyamata ku M'mawa kwa Africa. Pulojekitiyi idapereka upangiri pa utsogoleri wabwino, uphungu, maphunziro womenyera ufulu, kupanga ma ubale ndi ena komanso kupereka thandizo loyambira.

Pepala ili likubweretsa pamodzi ndondomeko ya zoyenerera zokhudza umoyo wa mmaganizo zochokera kwa atsogoleri a Sawa. Kuchokera ku ukadaulo wawo komanso kugwira ntchito kwawo, zomwe akukumana nazo, zomwe akudziwa za chikhalidwe komanso mayankho omwe adapanga kudzera ku Pulojekiti ya Sawa.

TIKULIMBIKITSA:

- [ ] Ndondomeko zomwe zimafika ku madera, zopangidwa limodzi ndi achinyamata kuchokera pachiyambi.
- [ ] Thandizo la zachuma lomwe ndi lopezeka kwa mabungwe omwe akuyendetsedwa ndi achinyamata komanso lolimbikitsa ukadaulo wawo kuti apitirize ntchito yawo kuposera pa thandizo lobwera pakamodzi.
- [ ] Kafukufuku amene achinyamata komanso anthu a m'madera adzakhalemo kugwira ntchito limodzi popeza zofunika kudziwa.
- [ ] Ma ubale omwe amapereka mphamvu komanso kuthandizira umoyo wa achinyamata omwe akugwira ntchitoyo.
- [ ] Njira zothandizira pa umoyo wa m'maganizo zokhazikika pa achinyamata komwe akupezeka kale.
- [ ] Njira zovomerezeka zofotokozera nkhani zomwe ndi zothana ndi kusalana, komanso zosintha madera athu kukhala malo opereka thandizo kwa achinyamata.

Lipoti lonse likukamba za nkhani za atsogoleri a Sawa, miyambi komanso zitsanzo kuphatikizapo zoyenera kuchita; kusonyeza zomwe zili zotheka pamene achinyamata akudaliridwa komanso kupatsidwa zoyenerera kuti atsogolere.

PEZANI LIPOTI LONSE (KU LINKI IYI): kofiannanfoundation.org/ubuntuinaction

Kofi Annan Foundation · MCW · YMCA Africa Alliance · Funded by Wellcome